. ***Ndinachimwira kumwamba ndi pamaso pano, sindiyeneraso konse kutchulidwa mwana wanu"*** Gawo la Mulungu pa chipulumutso Pali kulapa(Machitidwe 2:38). Akhristu ochimwa amafunikira alape (Machitidwe 8:22). Mulungu amapereka ufulu kwa munthu: kulapa Kapena chionongeko (2 Petro 3:9; Luka 13:3). Kulapa kumaphatikiza kutuluka mu uchimo. Izi zimaoneka mu 1 Akorinto 6:9-11 pamene Paulo ananena mndandanda wa machimo umene anthu aku Korinto amachita asanave mau a Uthenga Wabwino. Machimo amenewo kuphatikizapo dama, chigolo, kukwatirana amuna kapena akazi okhaokha, kuba ndi zina zambiri. Paulo anati "***ndipo ena a inu munali otere, koma munasambitsidwa, koma munayeretsedwa.....***" (1 Akorinto 6 11). Amasambitsidwa ku machimo onse amene analapa. Ubatizo siumasintha banja losayenera ndi malemba kuti likhale mwa malemba chimodzimodzi kukwatirana amuna kapena akazi okhaokha munthu akabatizidwa ndikukhala wabwino ndi Mulungu. Kulapa kumaphatikiza zonse kuleka machimo ndi kubwerera kwa Mulungu. Kulapa ndikovuta chifukwa kumaphatikiza kusintha ndipo kusintha ndikopweteka kwambiri.

Pamene anthu akufunikira kuti alape pamene ali ndi chikumbumtima chotero amaumitsa mtima. ***"komatu dandaulirani nokha tsiku ndi tsiku , pamene patchedwa, Lero; kuti angaumitsidwe wina wa inu ndi chenjerero la uchimo***"(Ahebri 1:13). Kulapa kumakhudza kusintha mbali yathu. Chisankho ndi chomveka bwino, Kulapa kapena kuonongeka

FOR MORE INFO CONTACT;

rdgmissions@charter.net

www.icotb.org

KULAPA

Pamene uchimo unachititsa kuti zipata za ku paradiso zitsekedwe kwa munthu, khomo la kulapa linatsegulidwa kwa iye. M'masiku a chipangano chakale Mulungu amaitana anthu ku kulapa kudzera mu uthenga wa aneneri (Ezekiele 18:30; Yeremiya 18:1-8). Yohane m'batizi anatumidwa kudzalalikira za uthenga wa kutembenuka mtima kukonza njira ya kwa Khristu (Mateyu 3:1-2; Marko 1:4). Masiku ano Mulungu akulankhula nafe kudzera mwa mwana wake (Ahebri 1:1) ndipo Khristu akufuna uthenga wakutembenuka mtima ndi kukhululukidwa kwa machimo alalikidwe ku dziko lonse (Luka 24:46-47).

Mu m'chipangano chakale muli mawu osiyana a chiheberi amene amagwiritsidwa ntchito ku chingerezi pofuna kutanthauza "kulapa". Mawu a *''nacham''* nthawi zina amagwiritsidwa ntchito pakunena za Mulungu ndi pena za anthu. Mawu amenewa samagwiritsidwa ntchito pakunena za tchimo, ngakhale tchimo limapezeka nthawi imene tikunena za anthu. Mawuwa amatanthauza kulira,kumva chisoni. Kuphatikizapo chifundo, kukhumudwa kapena kupweteka. Ndimomwe ziriri mu Genesis 6:6: ***"ndipo Yehova anamva chisoni chifukwa anapanga munthu padziko lapansi, ndipo anavutika m'mtima mwake."*** Anagwiritsidwaso ntchito pa Yona 3:10; ***"Ndipo Mulungu anaona ntchito zao, kuti anabwera kuleka njira yao yoipa; ndipo Mulungu analeka choipa adanenachi kuti adzawachitira,osachichita."*** Mulungu samachita cholakwika koma amasintha zomwe amafuna kuchita chifukwa anthu alapa.

Ndiye pali mawu a chiheberi *''shawb''.* Mawu amenewa amatanthauza kubwerera kapena kusintha. Mawu amenewa amagwiritsidwa ntchito pafupipafupi ndi aneneri. Mawu amenewa amanena za kusintha khalidwe kuchoka ku tchimo ndi kubwerera kwa Mulungu. Mu 1 Mafumu 8:47

mabuku ena anagwiritsa ntchito mawu a ***"akakumbukira mitima yao"*** , mawu amenewa mu chiheberi ndi *shuwb*. Mawu amenewa anagwiritsidwaso ntchito mu Ezekiele 14:6: ***"Chifukwa chake uziti kwa nyumba ya israyeli, Atero Ambuye Yehova, Bwerani, lekani mafano anu, tembenuzani khope zanu kuzisiya zonyansa zanu zonse."*** Vesi imeneyi mwachindunji imati ***"bwererani kuchoka ku mafano anu."*** Izi zikungotanthauza kubwerera kusiya mafano ndi kutembenukira kwa Mulungu. Nkhani yofanana ndi iyi imapezeka mu Ezekiele 18:30. Anthu anauzidwa kuti ***"bwererani, nimutembenukire kuleka zolakwa zanu zonse."*** Sizinali zabwino konse nthawi imeneyo ngakhale pano kuleka zoipa. Munthu amafunika atembenuke kuleka zolakwa ndi kubwerera kwa Mulungu kuti alape.

Mu m'chipangano chatsopano mawu achigiriki *''metallomai''* amagwiritsidwa ntchito pakusonyeza kukhudzidwa. Awa ndi mawu amene amagwiritsidwa ntchito pokamba za Yudasi mu Mateyu 27:3. Yudasi anakhudzika mumtima mwake koma sanalape. Mawu achigiriki a *metanoeo* amafotokoza za kusintha muuzimu ndi kubwerera kwa Mulungu. Amenewa ndi mawu amene anagwiritsidwa ntchito mu Mateyu 3:2: ***"Tembenukani mitima chifukwa Ufumu wa kumwamba wayandikira."*** Amenewanso ndi mawu amene Petro adagwiritsa ntchito mu Machitidwe 2:38:***" lapani batizidwani yense wa Inu***"

Kufunika kwa kulapa kumaoneka mu m'ndime zotsatirazi. ***"Ndinena kwa inu, Iaitu; koma ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo"*** (Luka 13:3). Kumwamba kumakhala chimwemwe pamene munthu alapa ***"Ndinena kwa inu, kotero kudzakhala chimwemwe kumwamba chifukwa cha wochimwa mmodzi wotembenuka mtima,koposa anthu olungama makumi asanu ndi anai mphambu zisanu ndi anai, amene alibe kusowa kutembenuka mtima."*** (Luka 15:7). Kulapa kumalamulidwa ndi Mulungu. ***"Nthawi za kusadziwako tsono Mulungu analekelera; koma tsopanotu alikulamulira anthu onse ponseponse atembenuke mtima"*** (Machitidwe 17:30). ***Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena achiyesa chizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu; wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa"*** (2 Petro 3:9).

Zikuoneka kuti pali kusamvetsetsa padziko lapansi za nkhani yokhudza kulapa. Kuona molakwika kulapa simantha. Mu Machitidwe 24:25 Felikisi anagwidwa ndi mantha koma palibe pamene analapa. Kulapa sikukhala ndi mantha ndi ntchimo, 2 Akorinto 7:10 imanena kuti chisoni cha kwa Mulungu chitembenuzira mtima ku chipulumutso. Zimaoneka kuti Yudasi anangochita chisoni pazimene adapanga koma sanalape.

Kuona molondora kulapa ndi kusintha kwa cholinga cha munthu chifukwa cha chisoni cha kwa Mulungu kutsatira kusintha kwa moyo. Pali zitsanzo ziwiri zabwino zokhudza kulapa zimene zimaoneka m'mawu a Mulungu. Choyamba, ganizirani za anthu aku Ninive. "***Anthu aku Ninive adzauka pamlandu pamodzi ndi obadwa amakono, nadzawatsutsa; chifukwa iwo anatembeneka mitima ndikulalikira kwake kwa Yona. Ndipo onani wakuposa Yona ali pano"*** (Mateyu 12:41). Uthenga wa Yona unali uthenga wa chiweruzo ku Ninive. "***Ndipo Yona anayamba kulowa mzindawo ulendo wa tsiku limodzi, nalalikira, nati, atsala masiku anai ndipo Ninive adzapasuka"***(Yona 3:4). Anthu analalikira kusala ndi kuvala ziguduli. Kulapa kwawo kudaoneka ndi Mulungu komaso anthu. "***Ndipo Mulungu anaona ntchito zao, kuti anabwera kuleka njira yao yoipa"*** (Yona 3:10). Anabwelera kuleka njira yao yoipa ndi kupita kwa Mulungu; uku ndiye kulapa kwenikweni.

Chitsanzo chachiwiri chimaoneka mu fanizo la mwana wolowelera Luka 15:11-32. Atachoka kwa Atate ake ndikuononga chuma chake ndi makhalidwe achitayiko. Vesi 17 ikuti **"koma *mmene anakumbukira mumtima***." Chimene chikupezeka mu kulapa kwake ndi chiyani? choyamba, anakumbukira kumene anali. Anadziona yekha akuweta nkhumba. Keneka, pali chisoni chenicheni pa tchimo lake. Ndipo anati adzanyamuka ndikudzapita kwa Atate ake. Kuphatikizapo izi kunali kudziwa ntchimo lake. Mu vesi 18 adati "**Atate ndinachimwira kumwamba ndi pamaso panu"** Tikuonaso umunthu mu vesi 21**. "**